

# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa  
kuchokera m'Baibulo kupita kwa  
amene akulalikira Uthenga Wabwino

## TEMBERERO LA IMFA

*Koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa usadye umenewo; chifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu.*  
—Genesis 2:17

Pachiyambi, Mulungu analenga munda wokongola wa Edeni kwa Adamu ndi Heva kuti adzisangalalamo komanso ngati malo amene Iye adziyanjana nao. Yehova Mulungu anaika mtengo wopatsa moyo ndi mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa mkati mwa mundamo (Genesis 2:9). Pamene Adamu ndi Heva anadya za mu mtengo wa moyo, umoyo wao ndi mphamvu zao zinasungika. Iwo analengedwa ndi mizimu yosafa ndi yamoyo, ndipo Mulungu anapangiratu kuti iwowo adzakhale amoyo kuthupi mpaka muyaya. Ngakhale zinali choncho, Mulungu anawalamula kuti asadzadye za mu mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa. Chilango cha kusamvera kumeneku chinali imfa. Mulungu anawapanga anthu kuti akhoza kumaganiza paokha komanso anawapatsa iwo mphamvu zosankha chimene chili choyenera kuchikonda.

Adamu ndi Heva anagonjera ku yesero la mdaniyo ndipo anadya chipatso cha mtengo umene anawakaniza uja. Pamene iwo anachita tchimo ili kapena kusamvera kumeneku, maso ao anatseguka ku zoonadi zenizeni za chabwino ndi choipa (Genesis 3:6-7). Chidziwitso chimenechi chinawalanda kwamuyaya anthuwo mtima wosadziwa choipa umene analengedwa nao. Asanachimwe, Adamu ndi Heva anali mu nyengo yakusadziwa chabwino ndi choipa komanso anali ndi chiyero chazimu.

Mulungu anachitadi monga mwa Mau ake popeza chimene Iye ali lero ndi chimene adzakhale mtsogolomo. Imfa ija imene Mulungu anayilengeza m'mundamo inakwaniritsidwa. Kodi imeneyi inali imfa

yotani? Temberero la imfa linali mu magawo awiri—kuuzimu ndiponso kuthupi.

Imfa ya kuuzimu inabwera ndipo panali kusiyantsidwa pakati pa Mulungu ndi munthu. Mulungu ali Mulungu woyera ndipo sangakhale m'chiyanjano ndi izo zimene sizili zoyera. Chiyanjano ndi ubale wauzimu zimene zinalipo pakati pa Mulungu ndi munthu zinaonongeka chifukwa cha uchimo. Mtima wa munthu unadetsedwa ndi chidziwitso cha zabwino ndi zoipa zimene zinabwera chifukwa cha kuchimwa kwa Adamu. Ndipo ngakhale masiku ano, ana sitifunika kuwaphunzitsa kuchita zoipa popeza mwachibadwidwe mitima yao ili yopotokera kale ku uchimo. Mfumu Davide ananena za izi mu Masalmo 51:5 pamene anati, "Onani, ndinabadwa m'mphulupulu, ndipo mai wanga anandilandra m'zoipa." Davide amanena ndi kuvomereza za chikhaliidwe cha uchimo chimene iye anali nacho kuchokera kuchiyambi. Mfundo imeneyi imadziwika ndi mau akuti "tchimo lobadwa nalo" imakamba za chilakolako choipa chachikulu komanso mtima wopotokera ku uchimo umene aliyense amabweretsa kudziko lino panthawi imene iye akubadwa.

Pakhala pali matsutsano ambiri ndi kugawanikana kochuluka pa chimene chimayambitsa kapena kupitiriza chikhaliidwe chauchimochi chimene chinayamba m'munda wa Edeni ndipo chimafalikira ku mibadwo yakudza pambuyo. Pamapeto pa kukambirana komanso mtsutso uliwonse, munthu amene akufunafuna choonadi akuyenera kuvomereza zenizeni zimene zikunenedwa pa Aroma 3:23, "pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemere wa Mulungu." Chizolowezi komanso mchitidwe wa munthu wosaombedwa ndiwo wopendekekeru ku zinthu zathupi zauchimo. Kupyolera mu mwazi



"Temberero la imfa  
linali mu magawo  
awiri—kuuzimu  
ndiponso kuthupi."

Mau a Mkonzi

Kalozera posanthula  
Baibulo: Imfa ndi  
kuuka, koyamba ndi  
kwachiwiri

Imfa ndi kuuka  
koyamba ndi  
kwachiwiri

Funso Yankho

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

# ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

## Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

## Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

## Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

## Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;  
Aef. 2:1, 5-6

## Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

## Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

## Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;  
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

## Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

## Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;  
Akol. 1:18

## Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

## Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;  
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

## Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

## Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;  
1 Akor. 7:10-11

## Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

## Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;  
Mat. 25:31-46

## Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

## Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

## Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

wa Yesu ndiponso mphamvu yakuyetsa ya Mzimu Woyera, munthu akhoza kubwezeretsedwanso mu ubale ndi Mulungu. Ngakhale kuti pali kuthekera kwakuti tikhoza kuchita uchimo chifukwa chakuti tili ndi mphamvu ya kusankha, komabe kukhumba kwa munthu woomboledwa kumakhakal kopendekekerana ku chilungamo.

“Chifukwa chake, monga uchimo unalowa m’dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa uchimo; chotero imfa inafikira



“**Temberero lomwelo  
la imfa linali ndi  
zotsatira zauzimu  
komanso zakuthupi.**”

anthu onse, chifukwa kuti onse anachimwa.” (Aroma 5:12). Imfa ya nthawi yomweyo imene inachitika kwa Adamu ndi Heva inali yauzimu. Popanda chikhululukiro ndiponso kuyetsedwa, munthu ali wotayana ndi Mulungu mu imfa ya kuuzimu. “Koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo machimo anu abisa nkhope yake kwa inu, kuti Iye sakumva” (Yesaya 59:2).

Temberero lomwelo la imfa linali ndi zotsatira zauzimu komanso zathupi. Ngakhale kuti mzimu wa munthu unali wosafa, Mulungu analengeza kuti “chifukwa kuti ndiwe fumbi, ndi kufumbiko

udzabwerera” (Genesis 3:19). Limeneli silinali dongosolo la Mulungu la poyambirira, koma linafika pamene Adamu anachimwa, “Ndipo anamuingitsa munthuyo; nakhazika akerubi cha kum'mawa kwake kwa munda wa Edeni, ndi lupanga lamoto lakuzungulira ponsepo, lakusunga njira ya ku mtengo wa moyo” (Genesis 3:24). Kuyambira pa nthawi imene Adamu ndi Heva anapirikitsidwa ku munda uja ndipo analetsedwa kuti asadye za mu mtengo wamoyo, matupi ao anasiya kutsitsimutsidwa ndipo matupiwo anayamba kuonongeka. Kukhala ndi moyo wautali kwa thupi lao lanyama kukuoneka kuti kumatengera zakuti iwowo adye zipatso za mu mtengo wamoyo. Zipatso zake zimalimbitsa thupi ndi kuliteteza kuti lisaonongeke. Kuyambira pa nthawi ya uchimo wa Adamu, nthawi ya munthu yokhala ndi moyo kuthupi inachepetsedwa.

Temberero la uchimo linali imfa ya kuuzimu ndi kuthupi. “Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa” (Aroma 6:23). Imfa yauzimu ndiponso imfa yakuthupi zonse pamodzi zinali zotsatira za uchimo wa Adamu ndipo zimenezi zinafalikira kwa anthu onse. Imfa yakuuzimu ndiyo kulekanitsidwa ndiponso kusiyana kwa mzimu wathu pamaso pa Mulungu chifukwa cha kusalungama. Imfa yakuthupi, imene imatanthauza kuti kusiya kugwira ntchito kapena kusatakataka kwa thupi, inabwera chifukwa cha kuchimwa. Kulengeza za imfa kunali kumodzi, koma zotsatira zake zinali m'magawo awiri ndipo zokhudza mibadwo-mibadwo. ■

*Gospel Truth* ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kutu mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa [www.thegospeltruth.org](http://www.thegospeltruth.org) ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA  
[editor@thegospeltruth.org](mailto:editor@thegospeltruth.org)

# Mau a Mkonzi



*Pakuti monga imfa inadza mwa munthu, kuuka kwa akufa kunadzanso mwa munthu.*  
—1 Akorinto 15:21

Imfa inabwera kwa anthu kugawo lathupi komanso lauzimu chifukwa cha tchimo la Adamu, koma tiyamika Mulungu, chifukwa kudzera mwa Yesu Khristu, imfa inagonjetsedwa. Kufa kunabwera mwa Adamu, koma kukhalabe ndi moyo kunabwera mwa Khristu. Uchimo ndi imfa zilibenso mphamvu pa anthu chifukwa temberero linaphwanyidwa kudzera mu imfa ndi kuuka kwa Ambuye wathu.

Kalata ya Gospel Truth ya ulendo uno ikukamba za chiphunzitso cha imfa yoyamba ndi yachiwiri komanso kuuka koyamba ndi kwachiwiri. Ndapemphera, ndawerenga mabuku, ndachita kafukufuku wochuluka mu mitu imeneyi. Pali ziphunzitso zambiri zimene zili zabadza ndithu, popeza zimasutsana ndi ziphunzitso za Khristu. Ngakhale pamene ndafufuza zolembe zakale pa mutuwu kuchokera kwa abale a mpingo wa Church of God, ndapeza kuti pali maganizo osiyanasiyana okhudzana ndi matanthauzo ena ndi ena. Ena mwa abale amanena kuti imfa yoyamba ija inali imfa yakuthupi pamene ena amaphunzitsa kuti imfa yauzimu inachitika m'munda wa Edeni. Ziphunzitso ziwiri zonsezi zikugwirizana ndi matanthauzo komanso chiphunzitso zopezeka m'Malemba.

Ndafika potsimikizika ndipo ndili ndi mtendere wamumtima komanso m'maganizo kupyolera m'mau amene amati "imfa yoyamba" inabwera potsatira kulengeza kamodzi kumene Mulungu ananena ndipo kunali chilango cha kusamvera.

Kulengeza KAMODZI kokhako kunali kwathupi ndiponso kwauzimu. Khristu anabweza mphamvu ya temberero limodzi lija, limene linali mu magawo awiri, kudzera mu kuuka koyamba ndi kwachiwiri.

Ndikulimbikitsika ndi kukondwera ndi Malemba amene tagawana mu kalata ino. Pemphero langa ndilo lakuti wowerenga aliyense alimbikitsika kuti auke ku uzimu kupyolera mwa Khristu ndipo achenjezedwe za chenjezo lachiwiri ndiponso lomaliza la imfa imene ikudza kwa osakhulupirira pa tsiku la chiweruzo. Ndiyamika Mulungu kuti gehena alibe mphamvu pa iwo amene aukitsidwa mwauzimu.

Michael W. Smith

July 2019



*Mukafuna kutipeza*

*pa intaneti, mulembe*


*www.thegospeltruth.org*

*kuti mudzilandira makalata*

*athu kapenanso kuti*

*muone makalata akale.*

## Imfa yoyamba ndi yachiwiri komanso kuuka koyamba ndi kwachiwiri



# Kalozera posanthula Baibulo

## Mutu: Imfa ndi kuuka, koyamba ndi kwachiwiri

**Kuwerenga Malemba:** *Wodala ndi woyera mtima ali iye amene achita nao pa kuuka koyamba; pa iwowa imfa yachiwiri ilibe ulamuliro.* —Chivumbulutso 20:6a

**Mwachidule:** Tchimo la Adamu m'munda mwa Edeni linabweretsa temberero la imfa pa anthu. Imfa imeneyi, yomwe ili imfa yoyamba, inali yakuthupi ndi ya kuuzimu. Yesu Khristu anabwera kudziko lino lapansi kuti kupyolera mu imfa ndi kuuka kwake, anthu akhoza kukhala ndi yankho ku zotsatira za uchimo umene unali magawo awiri. Kuuka koyamba ndiko kuuka kwauzimu kumene kwachitika kupyolera mu chipulumutso ndiponso mu kuuka kwachiwiri kumene kuli kuuka kwenikweni. Kumeneku ndiko kuuka kwathupi komwe kudzachitike kumapeto a nthawi. Ngakhale kuti pali yankho pa imfa yoyamba ija, kwa iwo amene sanavomereze Khristu ndipo sakhala nawo mu imfa yachiwiri. Komatu palibe yankho ku temberero la imfa yachiwiri ndi yomaliza chimene chili chizunzo chosatha ku gehena.



### I. Zotsatira za uchimo m'munda wa Edeni

- A. Genesis 2:9 Mitengo iwiri yapadera m'munda mwa Edeni.
- B. Genesis 2:16-17 Ubwino ndi zotsatira za mitengo iwiriyo.

### II. Magawo awiri a Imfa

- A. Aroma 5:12 Imfa ndiyo chotsatira cha uchimo wa Adamu.
- B. Genesis 3:19 Imfa yakuthupi.
- C. Genesis 3:22, 24 Adamu sanaloledwe kukhudza mtengo wa moyo.
- D. Aroma 6:23 Mphoto ya uchimo ndiye imfa.
- E. Genesis 3:6-7 Kukhala osadziwa choipa kutanayika chifukwa cha uchimo.
- F. Masalmo 51:5 Munthu ndi wotayika kwambiri.
- G. Yesaya 59:2 Uchimo umatilekanitsa ndi Mulungu.

### III. Imfa yauzimu ndi kuuka kwauzimu

- A. Luka 15:24 Mwana wolowerera.
- B. Yohane 5:24-25 Anachoka ku imfa nalowa m'moyo.
- C. Aefeso 2:1, 5-6 Iwo amene anamwalira mu uchimo anadzutsidwa.
- D. Aroma 5:8-21 Imfa kudzera mwa Adamu. Chipulumutso kudzera mwa Khristu.
- E. Yohane 11:25-26 Moyo kudzera mwa Khristu.

### IV. Imfa yathupi ndi kuuka kwathupi

- A. Yohane 5:28-29 Kuuka kuchokera kwa akufa.
- B. 1 Akorinto 15:26 Imfa ndiyo mdani womaliza.
- C. 1 Akorinto 15:42-57 Kuuka kwathupi.

### V. Imfa yachiwiri

- A. Chivumbulutso 20:12-15 Imfa yachiwiri ndiyo chilango chamuyaya.
- B. Mateyu 22:13 Kulira ndiponso kukukuta mano.
- C. Luka 16:23-24 Gehena ndi malo a chizunzo.
- D. Marko 9:43-44 Moto wake ngwosazimika.

### VI. Iwo amene adzapezeke mu imfa yachiwiri

- A. Chivumbulutso 21:8 Osalungama.
- B. Chivumbulutso 2:11 Ogonjetsa sadzapwetekedwa.
- C. Chivumbulutso 20:6 Ilibe mphamvu pa oomboledwa.

### Kumaliza


*Iye wokhala nalo khutu amve chimene Mzimu anena kwa Mipingo. Iye amene alakika sadzachitidwa choipa ndi imfa yachiwiri.*  
—Chivumbulutso 2:11



# IMFA NDI KUUKA

## KOYAMBA NDI KWACHIWIRI

Imfa inali chilango cha uchimo chifukwa cha kusamvera m'munda wa Edeni. Mtundu umenewu wa "Imfa yoyamba" unali magawo awiri ndipo umakhudza imfa yathupi ndi yauzimu. Kulengeza kwa imfa kunali kwakanthawi, monga m'mene Yesu Khristu anachitira popereka njira kuti mzimu uwukitsidwe ku moyo ndiponso kuti uyanjanitsidwense ndi Mulungu. Mphamvu ya imfa yakuthupi nayonso inaonongedwa. Padzakhala kuuka kwathupi panthawi imeneyi ya kumapeto a dziko lino.



**"Chilango cha imfa yakuuzimu chinasinthidwa kupyolera mu chikhululukiro ndi chiweruzo cha Yesu Khristu."**

(Luka 15:24). Mwanayo sanali wakufa kuthupi ayi koma anali wakufa kuuzimu. Pamene anasiya moyo wake wauchimo, anakhalanso wamoyo. Iwo amene ali akufa ku uzimu amakhalanso amoyo kupyolera mu kuuka kwauzimu.

"Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga, ndi kukhulupirira Iye amene anandituma Ine, ali nao moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wachokera kuimfa, nalowa m'moyo. Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti ikudza nthawi, ndipo ilipo tsopano, imene akufa adzamva mau a Mulungu; ndipo iwo akumva adzakhala ndi moyo." (Yohane 5:24-25). Yesu samanena za iwo amene ali akufa kuthupi kapenanso za kuuka kwakuthupi. Iye amanena za uzimu wa munthu wochimwa amene wakhulupirira mwa Ambuye nakhala nawo moyo kupyolera mwa Mwana wa Mulungu. "Tingakhale tinali akufa m'zolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi ndi Khristu (muli opulumutsidwa ndi chisomo), ndipo anatiukitsa pamodzi, natikhazikitsa pamodzi m'zakumwamba mwa Khristu Yesu" (Aefeso 2:5-6).

### **Kuuka Koyamba (Kwauzimu)**

"Wodala ndi woyera mtima ali iye amene achita nao pa kuuka koyamba; pa iwowa imfa yachiwiri ilibe ulamuliro" (Chivumbulutso 20:6). Kuuka koyamba ndiko kuuka kwauzimu kumene kumachitika pamene wochimwa alapa machimo ake ndipo asandukanso wamoyo kupyolera mwa Yesu Khristu. Yesu anapereka chithunzithunzi chimenechi chopezeka mu nkhani ya mwana wolowerera amene anachoka kunyumba kwao ndipo anaphwanyanya ubale wake ndi atate wake. Pamene mwana wolowerera uja anabwerera, atate ake anakondwera, "chifukwa mwana wanga uyu anali wakufa, ndipo akhalanso wamoyo; anali wotayika, ndipo wapezedwa"

### **Imfa yauzimu yasuluka**

Pa Aroma 5:8-21 akuphunzitsa mwachimvekere kuti uchimo ndi imfa zinabwera chifukwa cha kulakwa kwa Adamu, koma kulungamitsidwa m'moyo zinabwera ndi Yesu Khristu Ambuye wathu. Munthu tsopano akhoza kuyanjanitsidwanso ndi Mulungu kupyolera mu imfa ndi kuuka kwa Mwana wake. Monga Yesu ananenera, "Ine ndine kuuka ndi moyo: wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo; ndipo yense wakukhala ndi moyo, nakhulupirira Ine, sadzamwalira nthawi yonse" (Yohane 11:25-26). Chilango cha imfa yakuuzimu chinasinthidwa kupyolera mu chikhululukiro ndi chiweruzo cha Yesu Khristu. Pamene gawo la uzimu la imfa yoyamba lasuluka kupyolera mu kuuka kwauzimu. Zimenezi zikulongoledwa momveka bwino pokamba za ubatizo wamadzi kuti timayikidwa m'manda ndi Khristu mu ubatizo ndipo timaukitsidwa kwa akufa kuti tiyende m'moyo wachiyero (Aroma 6:4-5). Ngakhale kuti si madzi amene amapulumsa, koma ubatizo uli chizindikiro cha kuuka chimene chimachitika pamene munthu apulumutsidwa ndi mwazi wa Yesu. Kuuka kwauzimu kumeneku kumatchedwa kuti kuuka koyamba, chifukwa ndi kumene kuli kumasulidwa kwa mzimu kuchokera ku imfa ya uchimo kupita ku moyo watsopano mwa Khristu.


### **Kuuka kwachiwiri (Kwathupi)**

Patsalira gawo lina lachiwiri la imfa yoyamba imene ili yathupi. Yesu anabwera kudzabweretsa moyo wathunthu ndipo anapereka njira yothana ndi imfa yoyamba ija. Mzimu unaukitsidwa ku moyo kudzera mu kuuka koyamba ndipo thupi la imfa lidzaukitsidwa mu kuuka kwachiwiri. "Musazizwe ndi ichi, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m'manda adzamva mau ake, nadzatulukira, amene adachita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adachita zoipa kukuuka kwa kuweruza" (Yohane 5:28-29). Kuuka kwa thupi kudzachitika pa tsiku la mtsogolo. "Mdani wotsiriza amene adzathedwa ndiye imfa" (1 Akorinto 15:26). Khristu anaipambana imfa ndi anaigonjetsa kudzera mu kuuka kwake. Pamene Yesu adzabweranso, padzakhala kuuka kwathupi, ndipo onse adzaimirira

*(Yapitirira pa tsamba 6)*

(Kuchokera pa tsamba 5)

pampando wa Mulungu wakuweruza. Thupili, limene likhoza kuonongeka ndi kufa lidzaukitsidwa lili losatha kuonongeka ndi losafa. Imfa idzamizidwa mu chigonjetso! (1 Akorinto 15:42-57).



“Pakuti monga imfa inadza mwa munthu, kuuka kwa akufa kunadzanso mwa munthu. Pakuti monga mwa Adamu onse amwalira, choteronso mwa Khristu onse akhalitsidwa ndi moyo” (1 Akorinto 15:21-22). Kuuka kwathupi kumeneku kumadziwikanso kuti kuuka kwachiwiri. Kulengeza kwa imfa kwakhala ngati chophimba pa munthu kuyambira pa nthawi ya Adamu; koma kudzera mwa Khristu, pali kuukitsidwa kuwiri kumene kumaphwanya ndi kusulutsa mphamvu ziwiri zimene zili mu imfa yoyamba ija. Kuuka koyamba kuja ndiko chipulumutso pamene kuuka kwachiwiri ndiko kuuka kwathupi kuchokera kwa akufa.

“Pali kulengeza kwachiwiri kwa imfa kuchokera kwa Mulungu kumene kuli komaliza ndi kwamuyaya; ndipo sipadzakhala mwayi wakuti munthu apulumuke ku chilango cha imfa.”

### Imfa yachiwiri ndiyo yamuyaya

Imfa yoyamba ndi yakanthawi kudzera mu mphamvu ya Khristu Yesu kwa onse amene adzipereka okha ku mphatso ya Mulungu. Pali kulengeza kwachiwiri kwa imfa kuchokera kwa Mulungu kumene kuli komaliza ndi kwamuyaya; ndipo sipadzakhala mwayi wakuti munthu apulumuke ku chilango cha imfa yachiwiri.

“Ndipo ndinaona akufa, akulu ndi ang’ono alinkuima kumpando wachifumu; ndipo mabuku anatssegulidwa; ndipo buku lina linatsegulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m’abuku, monga mwa ntchito zao. Ndipo nyanja inapereka akufawo anali momwemo, ndipo imfa ndi dziko la akufa zinapereka akufawo anali m’menemo; ndipo anaweruzidwa yense monga mwa ntchito zake. Ndipo imfa ndi dziko la akufa zinaponyedwa m’nyanja yamoto. Iyo ndiyo imfa yachiwiri, ndiyo nyanja yamoto. Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m’buku la moyo, anaponyedwa m’nyanja

yamoto” (Chivumbulutso 20:12-15). Imfa yachiwiri ndiyo ikidwa ndi Mulungu ndipo kumeneko kuli kusautsika, mdima komanso kuvutika. Imfa yachiwiri idzachitika pa chiweruzo cha kwa onse amene akana kuombedwa ku mphamvu ya imfa yoyamba ija kupyolera mwa Yesu Khristu.

### Palibe mankhwala opewera imfa yachiwiri

Gehena ndi malo a chizunzo chachikulu (Luka 16:23-24) ndipo ndi kunjira kwa mdima; kumeneko kudzakhala “kulira ndi kukukuta mano” (Mateyu 22:13). Gehena ndi malo okhalako kwamuyaya “kumeneko mphutsi yao siikufa, ndi moto suzimidwa.” (Mark 9:43-44). Sikudzakhala kupumula pa kuzunzika ndi kusautsidwa mu imfa yachiwiri. Sipadzakhala chiyembekezo cha mpulumutsi kapena mwomboli wina, popeza palibe mankhwala opewera imfa imeneyi.

Onse amene ali osapembedza ndi osapulumsidwa adzakhala pansa pa mphamvu yosatha ya imfa yachiwiri. “Koma amantha, ndi osakhulupirira, ndi onyansa, ndi ambanda, ndi achigololo, ndi olambira mafano, ndi onse a mabodza, cholandira chao chidzakhala m’nyanja yotentha ndi moto ndi sulufure; ndiyo imfa yachiwiri” (Chivumbulutso 21:8).

### Mupulumutsidwe kuti mupulumuke ku imfa yachiwiri

Tiyamika Mulungu, pali kupulumuka ku imfa yachiwiri kupyolera mwa Yesu Khristu. Ngakhale kuti anthu onse anali pansa pa mphamvu ya imfa yoyamba kuuzimu ndi kuthupi chifukwa cha tchimo la Adamu, anthu onse akhoza kuombedwa ku mphamvu ya imfa yoyamba ija kupyolera mwa Yesu Khristu. Imfa yachiwiri, yokakhala ku gehena kwamuyaya, idzakhala yopanda mphamvu pa iwo amene adzauke kuuzimu. “Wodala ndi woyera mtima ali iye amene achita nao pa kuuka koyamba; pa iwowa imfa yachiwiri ilibe ulamuliro” (Chivumbulutso 20:6a).

Mphatso ya Yesu Khristu inakonza zotsatira za imfa yoyamba ija ndipo imapereka chitsimikizo cha kumasuka kwathunthu kuchoka ku imfa yachiwiri. Vomerezani nsembe yopepesera machimo ya Yesu ndipo landirani chipulumutso chachikuluchi. Tsiku lililonse muyende mu mapazi a Ambuye wathu ndipo mukhale m’moyo woyera wokondweretsa Atate. Kumwamba kukudikira iwo onse amene akumana ndi kuuka kodabwitsa komanso kwauzimu ndipo adutsa kuchokera ku imfa kupita ku moyo. Lonjezo lake lili lokhazikika ndi lonjezoli lili lotsimikizika kuti: “Iye amene alakika sadzachitidwa choipa ndi imfa yachiwiri.” (Chivumbulutso 2:11b). ■



**Kodi 1 Atesalonika 4:13-18 akutiphunzitsa kuti kuuka kwa olungama kudzachitika pa nthawi zosiyana komanso pa nyengo zosiyana poyerekeza ndi osalungama? Zikuoneka kuti pakhoza kukhala kuuka kwathupi m'magawo awiri osiyana.**

Padzakhala kuuka kwathupi kuchokera kumanda kamodzi kokha. Pa Yohane 5:28-29 akutiphunzitsa mwachimvekere kuti: “Musazizwe ndi ichi, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m’manda adzamva mau ake, nadzatulukira, amene adachita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adachita zoipa kukuuka kwa kuweruza.” Posawerengera chiphunzitso cha aneneri ambiri onyenga, Yesu anati olungama ndi osalungama adzaukitsidwa mu ora lomwelo, kapena mu nyengo yomweyo. Izi zikusiyana ndi chiphunzitso chakuti tidzalamulira kwa zaka 1,000 pansi pano litatha dziko.

Pa 1 Atesalonika 4:16 akutiza kuti pamene Ambuye adzabweranso “akufa mwa Khristu adzayamba kuuka.” Akupitirizanso pa ndime 17: “pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m’mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse.” Ndime imeneyi ikupereka chithunzithunzi cha zimene zidzachitike ndi oyeramtima pamene Ambuye adzabwerenso. Sakunena za zimene zidzawachitikire oyipa mtima kapena kuuka kwao kupita ku chiweruzo monga m’mene Khristu ananenera pa Yohane 5. Pa 1 Atesalonika 4:13-18 analemba pofuna kuwalimbikitsa iwo amene anali ndi chiyembekezo mwa Khristu (v13) ndipo amafuna kutonthoza oyera mtima (v18).

Padzakhala kuuka kumodzi kwathupi padziko lonse pakubwera kwa Yesu Khristu.

**Chonde longolani mau a pa Chivumbulutso 20:5-6 makamaka polingalira zimene zinalembedwa zokhudzana ndi zaka 1,000.**

Ndime imene tikulingalira likunena kuti: “Otsala a akufa sanakhalanso ndi moyo kufikira kudzatha zaka chikwi. Ndiko kuuka kwa akufa koyamba. Wodala ndi woyera mtima ali iye amene achita nao pa kuuka koyamba; pa iwowa imfa yachiwiri ilibe ulamuliro; komatu adzakhala ansembe a Mulungu ndi a Khristu, nadzachita ufumu pamodzi ndi Iye zaka chikwizo” (Chivumbulutso 20:5-6).

Pamene tikulingalira za kumayambiriro kwa ndimeyi, tiyeni tikumbukire chiphunzitso cha Yesu mu Yohane 5:24-29 chokhudzana ndi kuuka kuwiri kumeneku. Kwina kunali kwa panopa ndiponso kwauzimu (ikudza nthawi ndipo YAFIKA TSOPANO), pamene kwachiwiri ndi kwa mtsogolo komanso kwathupi (nthawi IKUDZA).

Tsopano tiyeni tilingalire za funso limene tili nalo. Chivumbulutso 20:5-6 sakunena za kuuka kuthupi kwa matupi koma kwa miyoyo imene inaphedwa panthawi imene mpingo wa Roman Catholic ndi wa chi Protestant unali kulamulira. Ndime imeneyi sikuphunzitsa



kapena kunena za kulamulira kwa pansi pano kwa zaka 1,000. Vesi 4 ikunena za “mizimu ya iwo amene adawadula khosi chifukwa cha umboni wa Yesu.” Inali mizimu imeneyi, osati matupi a oyera mtima, imene inali kulamulira kumwamba pamene ambiri anasiya chikhulupiriro komanso chinyengo chochuluka m’nthawi ya zaka za mdima komanso kuposera apo. Zaka 1,000 zimenezi zisanafike, kapena kwa nthawi yaitali ndithu, mpingo woyamba unkaoneka pansi pano monga wogonjetsa ndi wopambana. Panthawi imene ambiri anasiya chikhulupiriro, unalitu mpingo wabodza pansi pano. Chifukwa cha ichi, chivumbulutso chinaperekedwa ku mpingo umene unali kulamulira kumwamba ngakhale kuti pansi pano unali utasiya chikhulupiriro. Mizimu ya iwo amene anali kulamulira inali ya iwo amene anakumana ndi mphamvu yosintha moyo yopezeka mu kuuka koyamba pamene analandira chipulumutso pansi pano iwowo asanaphedwe.


Kuuka koyamba si kwa okhawa amene anaphedwa m’mbuyomu chifukwa cha Khristu koma kunali kuuka koyamba kumene kunapangitsa mizimuyo kuti ilamulire limodzi ndi Khristu kusiyana ndi kugonjera ku mphamvu ya imfa yachiwiri, kapena chilango chosatha. Pamene zaka 1,000 zidzathe, kapena nthawi yaitali idzamalizike, mpingo udzaonekanso padziko lapansi uli wogonjetsa ndi wopambana.





KODI MUKUDZIWA?

Pa Chivumbulutso 22:1-2 akupereka chithunzi cha mtengo wamoyo ukutuluka kuchokera ku mpando wachifumu wa Mulungu. Mavesi atatu akunena kuti “sipadzakhalanso temberero lililonse.” Mwana wa Mulungu ali ndi kuthekera kolawa za mu mtengo wa moyo lero kumene kulibe imfa yauzimu. Ku mbali ina ya mtsinjewo, ku moyo wosatha, mtengo wa moyo umakula mwakuti oomboledwa onse akhoza kudya zipatso zake ndi kukhala ndi moyo wamuyaya pamaso pa Mwanawankhosa wa Mulungu.



Mau a Nyengo Yake

## TONSE TIDZASANDULIKA

*Taonani, ndikuuzani chinsinsi; sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika.*  
—1 Akorinto 15:51

Paulo analemba kwa oyera mtima a ku Korinto kuwalimbikitsa iwo kuti akhale okhulupirika kwa Ambuye. Ena adzakhala atafa ndipo enawo adzakhale ndi moyo panthawi ya kubweranso kwa Khristu. “M’kamphindi, m’kuthwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osavunda, ndipo ife tidzasandulika” (1 Akorinto 15:52).

Mwana wa Mulungu tamvera, kusintha kukubwera! Matupi athuwa amakalamba ndiponso kusauka ndi matenda ndipo izi ndi zoona ndithu kwa anthu ambiri. Potsirizira, thupili lidzafa ndithu ndipo lidzabwerera ku dothi popeza linalengedwa kuchokera kumeneko. Izi zili choncho chifukwa cha temberero la imfa limene linayikidwa pa anthu m’munda wa Edeni. Komabe, kwa woyera mtima wa Mulungu, temberero limenelo ndi lakanthawi. Yesu anagonjetsa imfa ndipo anaphwanya mphamvu ya temberero. Mulungu alemekezeke!



Pamene Yesu adzabweranso, akufa adzauka kuchokera m’manda ndipo anthu onse a Mulungu kuchokera ku mtundu uliwonse, chilankhulo chilichonse ndiponso mbadwo uliwonse adzasinthika. Kuuka kwakukulu ndi kwamphamvu kudzachitika padziko lonse lapansi ndipo ana ONSE a Mulungu adzalandira thupi laulemerero. Icho chimene chinali chakufa ndi chokutha kuwola chidzavala chosawola ndi chosafa.

Kusinthika kumeneku kudzachitika mkamphindi kochepe kwambiri ndiponso kudzakhala kwaulemerero. Monga Mulungu adzadzutsira akufa, chomwechonso Iye adzasintha amoyowo ndikukhala zolengedwa zosawola zimene sizingafe konse. Icho chimene chinali chofooka ndi chowonongeka kudzera m’moyo ndi imfa yakuthupi chidzalimbisidwa komanso chidzasanduka kukhala chosinthika ndi chatsopano.

Matupi athuwa sadzatha kuti ayime pamaso pa kukongola ndi ulemerero wa malo amene Mulungu watikonzera ife Kumwamba. Chifukwa cha ichi, Mulungu wakonzana kuti adzativeke thupi lina limene likhoza kupirira kwamuyaya mu ulemerero wa Kumwamba. Matupi athu osinthikawa, amene adzakhale nyumba ya mizimu yathu yamuyaya, sadzalawanso imfa. Mulungu anasankha kusatiwululira kuti thupi losinthikalo lidzakhala lotani makamaka, koma chimene tingadziwe ndi chakuti kusinthikaku kudzaposi izo zimene tingaziganizire m’matupi athuwa amene akhoza kufa. Mulimbikitsidwe mu moyo komanso poyembekezera imfa pamene inuyo nokha kapena ndi wokonedwa wanu mukuyenda mu chigwa chake cha imfa. Ngati munapulumsidwa ndi kusambisidwa mu mwazi, tsiku likubwera pamene mudzasinthika! ■

### Kuti Mutipeze

The Gospel Truth  
P. O. Box 2042  
Nixa, MO 65714  
USA

Email:  
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE